8. Kodi chimachitika nchiyani ku ntchito ya Mulungu ngati sitipemphera?

________________________________________

____________________________________________________

==========================================================

Timaona mphamvu ya Satana m'njira zambiri. Timaona anthu akuchiritsa odwala ndi mphamvu ya ziŵanda. Timaonanso akukopedwa ndi Satana kuti azipitirizabe kumamwa moŵa osakhoza kusiya. Timaona maiko onse komwe Akhristu akuzunzidwa chifukwa chakuti Satana ali ndi ulamuliro m'maikowo.

9. Kodi tingamenyane nayo bwanji mphamvu ya Satanayi?

____________________________________________________

==========================================================

10. Kodi tiyenera kupempherera zotani pamene tikuona mphamvu ya Satana?

________________________________________

____________________________________________________

==========================================================

M'phunziro lathu la Sabata ino tanenapo za zinthu zambiri zoyenera kupempherredwa. Kodi mungathe kuzikumbukira zonse? Mwina mwake zingakuthandizeni ngati mutaziganizira m'njira zinayi izi.

Tiyenera:
(1) Kudzipempherera.
(2) Kupempherera anthu otizungulira.
(3) Kupempherera mpingo.
(4) Kupemphera kuti chifuniro cha Mulungu chichitike.

11. Bvundikirani zinthu zimenezi ndipo mudziyankhire nokha osaonera.

==========================================================

*******************************************************************

MAYANKHO.

4. Mwa kupemphera.
2. Ayi.
10. Tiyenera kupemphera kuti chifuniro cha Mulungu chichitike.
8. Zinthu zina zimene Mulungu amafuna kuchita sizikuchitika.
1. Akhristu.
5. Ayi.
9. Mwa kupemphera.
3. Ayi, simungathe kulasa mzimu.
7. Ndi mtima wake wonse.
6. Kuti chifuniro chake cha Mulungu chichitike.

SABATA LACHISANU: KODI TIZIPEMPHERA BWANJI?
TSIKU LOYAMBA:

Tilibenso chifukwa china chonenera kuti sitidziŵa zoyenera kupempherera. Tatha sabata lathunthu tili kumanena za zinthu zinayi zina zosiyanasiyana zimene ife tiyenera kuzipempherera, kenaka mulembe zinthu zinanso pamunsi pake.

1. Tiyenera kudzipempherera. Kodi tiyenera kupempherera chiyani mwa ife tokha? ______________________________
______________________________________________

2. Tizipempherera anthu ena amene atizungulira. Kodi anthuwo ndi ayani? (Musaiŵale amene akutitsogolera ndiponso adani athu).

______________________________________________

3. Tizipempherera mpingo. Kodi woyenera kupemphereredwa mumpingo ndi ayani?

______________________________

4. Tizipemphera kuti Mulungu agonjetse mphamvu ya Satana m'dielekezi. Kodi ife tizipempha chiyani pamene tilikupempherera izi?

______________________________

==========================================================

Choncho, ife monga Akhristu tili ndi ntchito yaikulu. Ndiye ngatinso yatichulukira. Ntchito yopempherayi tidzaigwira bwanji? M'Buku Lopatulika tikupezamo ndime zambiri zotiuza za zimene tingapempherere. Komanso ndime zambiri zotiuza za kapempheredwe.

Taonani zomwe Mulungu anaŵauza anthu ake kupyolera mwa mneneri Yeremiya.

Yeremiya 29:13:

Ndipo mudzandifuna Ine, ndikundipeza, pamene mundifuna ndi mtima wanu wonse.

5. Ndi mawu ati mu m'ndimeyi amene amationetsa momwe tinayenera kumufunira Mulungu?

__________________________

===================================================

Kodi pali nthaŵi ina imene anthu amapemphera koma osati ndi mtima wawo wonse? Inde, nthaŵi zina amangopemphera ndi mawu apakamwa chabe. Iwo sapemphera zochokera pansi pa mtima. Amangopemphera chifukwa chakuti auzidwa osati chifukwa mitima yawo ikulilira kwa Mulungu.

6. Kodi tizipemphera bwanji? __________________________

===================================================

Pomwe Yesu amaphunzitsa ophunzira ake za pemphero mu Luka 18, taonani mmene anaŵaphunzitsira.

Luka 18:7:

...ndipo kodi Mulungu sadzachitira chilungamo osankhidwa ake akumuitana usana ndi usiku, popeza aleza nawo mtima?

7. Kodi ili likumveka monga pemphero lofooka lochokera mbali imodzi ya mtima?

____________________

===================================================

Pa mutu wokhawokhawu Yesu anafotokoza za m'Farisi ndi wamsonkho amene pemphero lake linayankhidwa. Onani mmene iye anapempherera.

Luka 18:13:

Koma wamsonkhoyo alikuima patali sanafune ngakhale kukweza maso ake kumwamba, komatu anadziguguda pachifuwa pake nanena, "Mulungu mundichitire chi-

fundo ine wochimwa.

8. Kodi muganiza kuti munthuyu anapempheradi ndi mtima wake wonse?

________________

==========================================================

Ndime inanso idzatithandiza kuona mmene timaonera tikamapemphera.

Ahebri 4:16:
Kotero tilimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wachisomo, kuti tilandire chifundo ndikupeza chisomo chotithandiza nthaŵi yakusoŵa.

9. Kodi ndime imeneyi ikuti tibwere bwanji kwa Mulungu?

________________________________________________

==========================================================

Mulungu safuna kuti tizikhala amantha kapena a mtima wopeleŵera pamene tikupemphera.

10. Kodi iye amafuna kuti tizipemphera bwanji? ___________

__________________________________________________

==========================================================

*******************************************************

MAYANKHO.

8. Ndiganiza anatero.
5. Ndi mtima wanu wonse.
2. Amayi, ana, abale ndi alongo, atsibweni ndi azakhali, achinansi, olamulira, ndi adani.
10. Molimba mtima, ndipo ndi mtima wonse.
7. Ayi.
4. Kuti chifuniro chake cha Mulungu chichitike.
1. Chakudya, zobvala, kupambana pa ntchito yanu, nzeru, chikondi, ndi mphamvu
9. Molimba mtima.
6. Ndi mtima wathu wonse.
3. Akulu ampingo, ndi Akhristu ena onse.

SABATA LACHISANU: KODI TIZIPEMPHERA BWANJI?
TSIKU LACHIWIRI:

Dzulo tinanena kuti tiyenera ndithu kutsimikiza zinthu zimene tikunena pamene tikupemphera. Mapemphero a mawu okha alibe mphamvu ndi Mulungu. Mulungu amamva tikamapemphera ndi mtima wathu wonse. Koma kumbukirani kuti kupemphera sikumuuza zinthu Mulungu.

1. Kodi pemphero ndi chiyani? ______________________________

______________________________

====================================================================

Ngati tikulankhula ndi Mulungu osati kumuuza zinthu kokha, koma tiyeneranso kumvetsera bwinobwino. Njira imodzi yochitira izi ndiyo kuwerenga Buku Lopatulika.

2. Kodi mawu amene ali m'Buku Lopatulika ndi andani?

______________________________________________

====================================================================

Mulungu amalankhula nafe kupyolera m'mawu ake amene ali m'Buku Lopatulika. Pamene tikuwerenga ndi kuganizira za Mawu ake ndiye kuti tili kumamvetsera. Pamene tili kuwerenga tingathe kumufunsa kuti atimasulire Mawu ake. Mulungu amanena kuti ngati ife tifunadi kumvetsetsa ndi kumvera Iye adzatisonyeza njira yake.

Yohane 7:17:

> Ngati munthu aliyense afuna kuchita chifuniro chake, (cha Mulungu) adzazindikira za chiphunzitsocho, ngati chichokeradi kwa Mulungu, kapena ndilankhula zochokera kwa Ine ndekha.

3. Kodi Mulungu adzatisonyeza njira yake ngati sitifuna kuchita zimene Iye amanena?

____________________

Tikatha kuwerenga Buku Lopatulika tingathe kupitirizabe kupempherera zinthu zimene tawerenga. Tingathe kumufunsa Mulungu chimene Iye akufuna kuti tichite nazo zinthu zimenezi.

4. Pamene tikupemphera tisamangolankhula kokha kwa Mulungu komanso tiyenera ku

____________________

==========================================================

Tsopano pano pali chinthu chodabwitsa kwambiri. Ngati tiyembekezera Mulungu kuti atilankhule pamene tili kupemphera Iye sadzangotiuza kokha chochita, koma adzatiuza zakuti tizipempherera. Adzatitsogolera ngakhale pamene tili kupemphera. Ngati titakumbukira zimenezi, zidzatithandiza kwambiri. Nthaŵi zina timabvutika m'mapemphero athu. Sitidziŵa bwino zimene tizipempherera kapena mmene tingapempherere. Kupyolera mwa Mzimu Woyera, Mulungu amatithandiza kupemphera.

Aroma 8:26:

> Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufooka kwathu, pakuti chimene tizipempha monga chiyenera, sitidziŵa; koma Mzimu mwini atipempherera ndi zobvuta zosatheka kuneneka.

5. Penyetsetsani bwinobwino pa ndime iyi. Kodi ndani amene ali kutipempherera pamene ife tili kupemphera?

____________________

==========================================================

Mulungu adzatichitira zinthu zonsezi ngati titapemphera ndi mitima yotseguka, kuyembekeza kuti Iye alankhule nafe.

6. Kodi muli kuona kuti kupemphera kumaposa kupempha zinthu kwa Mulungu?

____________________

==========================================================

Pamene tipemphera m'njira imeneyi, zinthu zidzabwera mwachionekere m'mitima mwathu zimene tiyenera kuzipempherera. Sitidzangopempherera zinthu zotikondweretsa kokha. Sitidzangopempheranso pemphero lalitali pa kupempherera anthu onse amene ali odwalawo kuti apeze bwino, koma tidzayamba ndi kupempherera zinthu zapadera ndi zinthu zenizeni zimene Mulungu amationetsa.

7. Pamene mupempherera anthu onse odwala, kodi mumayembekeza Mulungu kuti awachiritse anthu onsewo?

________________

==========================================================

Mwaona, nthaŵi zina mapemphero athu amangokhala akuluakulu ndiponso ataliatali kotero kuti amangokhala mawu okhaokha ndipo sitiyembekeza kuona mayankhidwe ake pamaso pathu. Koma ngati titapempha Mulungu zimene tingapempherere ndikupempherera zinthu zapadera kenaka tingathe kudikira mayankho ake.

8. Kodi muganiza kuti Mzimu Woyera adzatiuza kuti tipempherere anthu odwala onse nthaŵi imodzi?

________________________

==========================================================

Tiyeni tiyembekeze Mulungu kuti alankhule nafe pamene tikupemphera. Tiyeni timufunefune kuti atitsogolere ngakhale pa zimene tikuzipempherərazo. Nthaŵi zina adzatiuzanso chochita kuti mapemphero athu ayankhidwe. Tiyeni tinene kuti muli kupempherera munthu wina amene sali m'Khristu (wakunja) kuti atembenuke mtima, pamene mukupemphera ndikumvetsera mwina Mulungu angathe kukuuzani kuti mupite kukamuyendera ndikukamusonyeza chikondi chanu.

9. Ngati mukupempherera wina amene amakudani chifukwa chakuti mudanenerana mawu okwiitsana naye, kodi Ambuye adzakuuzani kuti muchite chiyani?

________________________________

________________________________________________________

==========================================================

Kupemphera sikungonena kokha mawu kwa Mulungu. Pali mbali ina ya pemphero imene ili yofunikanso kwambiri.

10. Kodi ndiyenera kuchita chiyani pamene ndili kupemphera kupatulapo kumuuza Mulungu zinthu?

______________________________

==========================================================

**********************************************************

MAYANKHO.

8. Sindiganiza choncho. Ndiganiza kuti adzatisankhira m'modzi kapena aŵiri akuti tiziŵapempherera molimbika poŵatchula aliyense dzina lake.
5. Mzimu Woyera.
2. Mawu a Mulungu.
9. Kupita kukamuyendera ndikukamupepesa chifukwa cha mawu amene munamulankhulira.
6. Ndikhulupirira kuti mumatero.
3. Ayi.
10. Ndiyenera kumvetsera.
7. Anthu sayembekezera kuti Mulungu achiritsa odwala onse ndi kutulika m'chipatala pa nthaŵi imodzi pamene akuŵapempherera.
4. Mvetserani kwa Mulungu.
1. Pemphero ndiko kulankhulana ndi Mulungu.

SABATA LACHISANU: KODI TIZIPEMPHERA BWANJI?
TSIKU LACHITATU:

Takhala tikulankhula za kupempherera kuchokera pansi pamtima wathu. Taphunziranso za mmene tingaganizire pamene tikupemphera.

1. Lembani mawu owerengeka a zimene mwaphunzira sabata ino za mmene tingapempherere.

______________________________________________

______________________________________________

==============================================================

Izi ndizo zinthu zimene zili mkati mwathu. Nanga bwanji zinthu zimene zili kunja kwathu? Lero tikufuna kunena za zinthu zimenezi. Kodi tiyenera kukapempherera kuti? kodi tiyenera kupemphera choima kapena chogwada? Kodi tiyenera kugwiritsa ntchito mawu ati? Ngakhale kuti zinthu izi siziri zofunika kwenikweni monga zoganizirika za mtima, Buku Lopatulika limatipatsa ziphunzitso zina za zimenezi.

Pamene Yesu anali kuphunzitsa ophunzira ake pa phiri tsiku lina, Iye ananena zinthu zambiri za mapemphero. Tamva kale mmene Yesu ananenera kuti tizipita tokha ndikukapemphera Iye mwa m'tseri.

Mateyu 6:6:

> Koma iwe popemphera, loŵa m'chipinda chako, nutseke chitseko chako, nupemphere Atate wako ali m'tseri, ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe.

2. Kodi ndime iyi ikuti tizikapempherera kuti? ____________

==============================================================

Koma mwina mwake inu mulibe chipinda chakuti mungatsekedwemo, kuti anthu ena asalowemo. Kodi izi zikutanthauza kuti simungathe kupemphera bwino? Ayi. Kumbukirani kuti chipinda simalo okhawo oti mungathe kukhala nokha opanda anthu ena ndikupemphera nokha kwa Mulungu. Anthu amene akhala

kunja kutali ndi mizinda angathe kupeza malo kuthengo kapena kuseri kwa chulu. Yesu anatisonyeza kachitidwe kake ka zimenezi.

Marko 1:35:
Ndipo m'maŵa mwake anauka usikusiku, natuluka namuka kuchipululu, napemphera kumeneko.

Mateyu 14:23:
Ndipo pamene Iye anaŵauza makamuwo, anakwera m'phiri payekha, kukapemphera: ndipo pamene panali madzulo, Iye anakhala kumeneko yekha.

3. Kuchokera m'ndime izi, ndikumalo aŵiri ati kumene Yesu anapita kukapemphera?

________________________________

________________________________

==========================================================

Koma ngati mumakhala mu mzinda, mwina mwake njira imene mungakhalire panokha ndi Mulungu ndiyo youka m'mamaŵa pamene anthu ena asanauke. Kapena mukhoza kupemphera nokha usiku anthu atagona. Chinthu chofunika kwambiri m'chakuti mupeze malo anokha kuti muzilankhula ndi Mulungu masiku onse.

4. Lembani malo amene mungathe kupita ndikukakhala panokha ndi Mulungu.

______________________________________

==========================================================

Kutseka chitseko monga mmene Yesu anatiuzira kumatanthauza kuposa kukhala ndi chitseko cha matabwa. Kumatanthauzanso kuika kutali zinthu zonse za m'dziko lapansi zimene zikanabwera m'maganizo athu kuti tisapemphere. Ichi m'chifukwa chake ife timatseka maso athu tikamapemphera.

5. Pamene muli kupemphera, kodi mumakhala ndi bvuto loganizira zinthu zina zambiri mmene mukanayenera kupempherera?

Pa tsikulo Yesu ananenanso zinthu zina kwa ophunzira ake.

Mateyu 6:7:

> Ndipo popemphera musabwereze-bwereze chabe ayi, monga amachita anthu akunja, chifukwa ayesa adzamvedwa ndi kulankhulalankhula kwawo.

6. Kodi munamvapo anthu ena amene amapemphera mobwereza-bwereza mawu okhaokhawo mosalekeza, kapena kunena kuti "Atate" kapena "Mulungu" pambuyo pa mawu ochepa?

---

Salomoni anati pa Mlaliki 5:1-2:

> Samalira phazi lako popita kunyumba ya Mulungu; pakuti kuyandikira kumvera kupambana kupereka nsembe za zitsiru, pakuti sizizindikira kuti zili kuchimwa. Usalankhule mwathuku mtima wako, usafulumire kunena kanthu pamaso pa Mulungu; pakuti Mulungu ali kumwamba iwe uli pansi, chifukwa chake mawu ako akhale owere-ngeka.

Ngakhalebe, Yesu amene ali chitsanzo chathu, nthaŵi zina anali kupemphera usiku wonse kwa Mulungu. Nanga chabwino ndi chiti, mapemphero ataliatali kapena mapemphero afupi-afupi? Kusiyana kwake ndi njira yomwe ife timapempherera. Solomoni anati mawu athu asamakhala ofulumira koposa pamaso pa Mulungu. Ndikukhulupirira kuti Mawu a Yesu anaganiziri-dwa bwino usiku wonse uja kudzanso iye anali kulankhula ndi kumvetsera. Ngakhale zinali choncho, kunamtengera iye usiku wonse kuti atsirize. Mwina mwake ndi malowo anapangitsanso kusiyana. Solomoni anati mawu apang'ono ndiwo afunika m'tchalitchi. Yesu ana~~li ku~~pemphera yekha pa phiri paja.

7. Kodi ndi mapemphero aatali okha ndi obwerezabwereza amene amankondweretsa Mulungu?

---

Tikanali ndi chinthu chimodzi chakuti tinene. Umu ndi mmene timakhali popemphera. Tiyeni tione anthu a m'Buku Lopatulika amene ankapemphera ndi kuona zimene anali kuchita.

1 Mafumu 8:22:
Ndipo Solomo anaimirira kuguwa lansembe la Yehova pamaso pa msonkhano wonse wa Israyeli, natambasula manja ake kumwamba.

Mateyu 26:39:
Ndipo anamuka patsogolo pang'ono nagwa nkhope yake pansi, napemphera, nati "Atate, ngati nkutheka, chikho ichi chindipititire Ine, koma simonga ndifuna Ine koma Inu."

Marko 11:25:
Ndipo pamene muimirira ndi kupemphera, khululukirani ngati munthu wakulakwirani kanthu; kuti Atate wanunso ali kumwamba akhululukire inu zolakwa zanu.

Machitidwe 20:36:
Ndipo mmene ananena izi, anagwada pansi, napemphera ndi iwo onse. (Uyu anali Paulo ndi anzake ku Aefeso)

Luka 23:42:
Ndipo ananena, "Yesu ndikumbukireni mmene mulowâ Ufumu wanu." (Pemphero ili linapemphereredwa ndi mbala ija imene inakhomeredwa pamtanda pambali pa Yesu)

Mateyu 14:30:
Koma mmene iye anaiona mphepo, anaopa; ndipo pamene anayamba kumira, anayamba kupfuula, nati, "Ambuye, ndipulumutseni ine!" (Ili linali pemphero la Petro pamene anali kumira m'madzi)

8. Kodi pali njira zoposera imodzi za mmene tingakhalire pamene tikupemphera?

______________________________

==========================================================

Anthu a m'Buku Lopatulika anali kupemphera ena ali chiimire, ena chogwada, ena atagwetsa nkhope zawo, ena atakweza manja awo, ena atamira m'madzi, ndiponso ena atangopachikidwa pa mtanda. Palibe lamulo lakuti popemphera tizikhala motere ayi.

9. Kodi Mulungu amayankha mapemphero athu chifukwa cha mmene timakhalira popemphera?

______________________________

===========================================================

Komatu, anthu aŵa anafuna kusonyeza ulemu kwa Mulungu. Pamene kunali kotheka iwo anali kugwada kapena kuimirira pamaso pa Mulungu, m'njira imene anaiona kuti inali yabwino yosonyezera ulemu. Ifenso tiyenera kusonyeza ulemu kwa Mulungu m'njira imene ife tiiona kuti ndiyabwino.

10. Kodi ndi njira iti yakupemphera imene mungaganizire kuti imasonyeza ulemu wanu kwa Mulungu?

_______________

===========================================================

*************************************************************

MAYANKHO

6. Ndiganiza kuti munamva ngati ine.
9. Ayi.
3. Kumalo ayekha, mphepete mwa phiri.
5. Akhristu ambiri amapeza mabvuto ndi zimenezi.
8. Inde.
2. M'chipinda mwa nokha.
10. Yankhani mmene mungaganizire.
4. Mudzayankha nokha funso limeneli.
7. Ayi.
1. Tidzakambirana m'kalasi za funso ili.

SABATA LACHISANU: KODI TIZIPEMPHERA BWANJI?
TSIKU LACHINAYI:

Takambapo mbali ziŵiri za kupemphera. (1) Mmene timamvera mkati mwathu. (2) Chimene timachita kunja kwathupi pamene tikupemphera.

1. Pakuganizira za mmene timamvera mumtima mwathu, kodi tizipemphera bwanji? ____________________

   ____________________________________________

2. Taganizirani za kunja. Kodi tizipita kuti kokapemphera? ______________ Kodi tizigwada nthaŵi zonse popemphera? ________

---

Palinso chinthu china chimene Buku Lopatulika limatiphunzitsira molimbika ndithu za mmene tingapempherere. Pambuyo pake tidzaona kuti kupempheretsaku kuli ndi chifukwa chimodzi cha zifukwa zambirimbiri zimene ife sitionera mayankho a mapemphero athu nthaŵi zina.

Onani Luka 18:1:
   Ndipo anaŵanenera fanizo lakuti ayenera iwo kupemphera nthaŵi zonse, osafooka mtima.

3. Mwa ndime iyi, kodi tizipemphera bwanji? ____________

   ____________________________________________

---

Apa ndi pamalo pomwe timalepherera nthaŵi zonse. Timayamba bwino. Timapita kumaloko tokha tili ndi Mulungu. Timapemphera ndi mtima wathu wonse. Timabwera pamaso pa Mulungu opanda mantha. Timawerenga Mawu a Mulungu. Timayesa

kumumvetsera pamene tikupemphera. Timayesa kuchita zinthu zimene Iye amafuna kuti tizichita. Timapempha Mzimu Woyera kuti atilangize zinthu zimene tiyenera kupempherera. Timayesa kunena zinthu za pansi pa mtima wathu osati kumangobwereza-bwereza mawu. Koma nthaŵi zina sitiona mayankho a mapemphero athu mwa msanga. Timatopa ndi kupemphera kenaka timaleka.

4. Kodi mapemphero athu adzayankhidwa tikamapemphera mwa njira imeneyi?

________________

==========================================================

Ayi, Yesu anati tizingopitirizabe kupemphera osataya mtima. Koma ichi ndi chinthu chobvuta kuchichita, makamaka pamene sitiona mayankho a mapemphero athu, ndiponso pamenepa Mulungu amaoneka ngati kuti sakutimvera. Koma kumbukirani kuti Mulungu sanena kuti adzayankha mapemphero athu mwa msanga. Kunena zoona, iye amanena kuti nthaŵi zina tidzayembekezera.

Masalmo 27:14:
    Yembekeza Yehova; limbika, ndipo iye adzalimbitsa mtima wako; Inde yembekeza Yehova.

5. Ngati mayankho a mapemphero athu sabwera msanga, kodi tiyenera kuchita chiyani?

________________________________

==========================================================

Nanga tiyenera kuchita chiyani pamene ife tikuyembekezera? Yesu atanena mawu akuti tizingopempherabe osataya mtima, Iye anakambanso nthano yosonyeza zimene anali kutanthauza. Tsekulani Buku Lopatulika pa Luka 18 ndipo muyambe kuwerenga pa ndime 1 ndipo mulekeze pa ndime 8, kenaka muyankhe funso ili.

6. Kodi mkazi wamasiye uja anatani pamene amayembekeza woweruza kuti amuthandize?

________________________________

____________________________________________________________

Izi ndi zimene Mulungu amafuna kuti tizichita. Ngakhale Iye sali ngati woweruza woipa, koma amafuna kuti tizingopemphabe zinthu zimene tizisoŵa. Yesu anafotokozanso nthano ina kuonetsa izi. Tsegulani Buku Lopatulika pa Luka 11 ndipo werengani ndime 5 mpaka 9.

7. Kodi Yesu anali kuphunzitsa zotani muthano iyi?

___________________________________________

8. Kupatulapo zopemphera ndi mitima yathu yonse kudzanso kusachita mantha, kodi tiyenera kupemphera bwanji?

___________________________________________

==========================================================

**********************************************************

MAYANKHO

7. Kuti tipitirizebe kumpempha Iye.
5. Tiyembekezere.
3. Tipitirizebe.
1. Ndi mtima wonse.
8. Pakupitirizabe ndipo osalekeza.
6. Anapitirizabe kupempha chinthu chimene anali kuchifuna.
4. Ayi.
2. Kumalo kumene tingakhale tokha. Ayi.

SABATA LACHISANU: KODI TIZIPEMPHERA BWANJI?
TSIKU LACHISANU:

Dzulo tinaphunzira chimene tiyenera kuchichita ngati sitipeza mayankho a mapemphero athu mwa msanga.

1. Nanga tiyenera kuchita chiyani? ______________________

================================================================

Palinso chinthu china chichikulu chimene tiyenera kudziŵa pakupemphera. Ichi chinanenedŵa kwa ife poyera m'Buku Lopatulika.

Pa tsiku lomaliza, usiku, pamene Yesu asanapachikidwe, ananena zinthu zambiri kwa ophunzira ake. Iye anaŵauza kuti anali kuŵasiya, koma adzaŵatumizira oŵatonthoza kuti adzaŵathandize. Kenaka anaŵauza kuti ngati adzafuna chilichonse adzapemphe ndipo adzapatsidwa. Sananene ichi kamodzi kokha, koma ananena kambirimbiri.

Yohane 14:13-14:

> Ndipo chimene chilichonse mukafunse m'dzina langa, Ndidzachichita kuti Atate akalemekezedwe mwa Mwana. Ngati mudzapempha chilichonse m'dzina langa, ndidzachita.

Yohane 16:23-24:

> Ndipo tsiku limenero simudzandifunsa kanthu. Indetu, indetu, ndinena kwa inu, Ngati mudzapempha Atate kanthu, adzakupatsani inu m'dzina langa. Kufikira tsopano simunapemphe kanthu m'dzina langa; pemphani, ndipo mudzalandira, kuti chimwemwe chanu chikwaniritsidwe.

2. Kodi Yesu anauza ophunzira ake kuti azichita chiyani ngati akusoŵa kanthu?
______________________________

================================================================